


CHICHEWA – “The Two Roads

NJIRA ZIWIRI



KUSANKHA NJIRA

Pamene tinyamuka ulendo kupita kumalo achilendo, timafunsira njira imene tingathe kudzeram. Ife timayenda maso athu ali chire ndipo ngati tiona kuti tasochera, timabwerera msanga ndi kuyang'ana njira yabwino.

Tsiku liri lonse tonse tirinkuyenda kudutsa mdziko lino kupita ku moyo **WOSATHA**, ku malo kumene **SIKUDZATHA**, ndipo kumene sikudzasinthika pamene tifikako. **Kodi mulinkudziwa kumene muli kupitako?**

BUKU LOTITSOGOLERA IFE

Mulungu, mwa chifundo ndi chikondi chache, watipatsa ife Buku Lotitsogolera ndilo **BAIBULO**, limene litisonyeza ife mooneka bwino njira ya **KUMWAMBA**. Mawu amene alembedwa munkapepala kano atengedwa **M'BAIBULO**. Baibulo limati: “Mawu anu ndiwo nyali ku mapazi anga, ndi kuunika kwa panjira panga.” (Masalmo 119:105).

NJIRA YAIKURU

Muli anthu ambiri m'njirayo. “Chifukwa chipata chiri chachikuru chipita ku Gehena, ndipo njira yake iri yotakata, ndipo pali ambiri amene alowa pa njirayo.” (Mateyo 7:13). Ambiri a iwo maso awo atsekedwa ndipo sakuona. Sadziwa, kapena salabadira kuti ali pa njira yakuchiononkeko. Imene ukuganiza kukhala njira yabwino itha kukulondolera kuchiononkeko. Baibulo limati: “Iripo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka, koma matsiriziro ache ndi njira yakuimfa (Miyambo 14:12). Maganizo awo abisika mu mdima ndi Satana, mulungu woipitsitsa wa dziko lino (2 Akorinto 4:4).

AKATUNDU

Anthu oyenda mnjira imeneyi ndi **OCHIMWA**, “Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu (Aroma 3:23). Sitingathe kum'bisira Mulungu mngakhale tchimo limodzi. Pakuti munthu ayang'ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mumtima (1 Samueli 16:7). Akatundu oipa amangidwa kumbuyo kwathu. Ife sitingathe kupewa tchimo liri lonse ndi mphamvu zathu. Katunduyu amanka nalemerabe pamene nyenga ikupita ndipo mphotho yache ya uchimo ndi imfa (Aroma 6:23).

MOTO

Payenera tsono kukhala chilango cha uchimo monga Yehova ali chiyero ndi choonadi. Mawu a Mulungu amatiuza ife kuti kuli ng'anjo ya moto, kumalo a chilango chosatha kwa iwo osamvera Mulungu. Baibulo limati: “Oipawo adzabwerera kumanda, Inde amitundu onse akuiwala Mulungu” (Masalmo 9:17). Sudzafunika kuti ukhale woipa kwambiri kuti upite kumeneko-Kuli kwa iwo amene aiwala Mulungu amene akonda matupi awo ndiponso kuti zinthu zonse ziri za dziko lapansi (Afilipi 3:19).

Mulungu ndi Mulungu wa chikondi amene safuna anthu ake aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa (2 Petulo 3:9). **Mwa chifundo ndi chikondi chache chachikulu, Mulungu wapanga** njira yothawirapo kwa onse amene aifuna njirayi. Kodi mufuna kupeza njira ya moyo?

NJIRA YA MOYO: MPULUMUTSI

Pakuti sitikadadzzipulumutsa tokha ku machimo kapena kuchilango choona cha machimo athu, **Mulungu adatipatsa Mpulumutsi**. “Pakuti Mulungu anaconda dziko lapansi kwambiri, koteri kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira lye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.” (Yohane 3:16). Mulungu, Atate wa Kumwamba anatuma Mwana wache m'modzi yekha Ndiye Ambuye Yesu Khirisitu kuchokera kumwamba kudza ku dziko lino lapansi. Iye anakhala monga ngati munthu wamba, koma sanachimwe ayi. Yesu anayenda-yenda kuchita zabwino: Kuchiritsa odwala, kuyeretsa akhate, kuchotsa ziwanda, kukhululukira olapa zochimwa zawo ndi kuphunzitsa anthu za Mulungu.

Koma cholinga chache chachikulu, kukhala munthu chinali kudzafa monga mwa nsembe ya ife tonse; Kupereka moyo wache wosachimwa ndi kukhetsa mwazi wache wa mtengo wa patali kulipira chilango cha machimo athu. Iye analola anthu wamba kuti amutenge lye, kumkwapula lye mpaka kusana kwacha kunatuluka magazi ndi mikwingwirima, ndi kumveka chibakuwa cha minga-minga pa mutu pache, ndipo potsiriza anamkhomepera lye pamtanda manja ndi mapazi omwe, pamene anapachikidwa osalimba-limba koma akumva ululu ndi kupweteka. Yesu Khirisitu Ambuye athu anasenza machimo athu mwini yekha m'thupi mwache pa mtanda (1 Petulo 2:24). Iye anamfera inu ndi ine.

KUUKA KWACHE

Patangopita masiku atatu ali m'manda, Yesu Khirisitu anauka kwa akufa. Iye anayenda-yenda ndi kuyankhulandi ophunzira ache kwa masiku makumi anayi ndipo iye anakwera kumwamba, nakukhala kudzanja la manja la Mulungu (Aroma 8:34). Mpulumutsi wa moyo wokhala ndi ulamuliro ndi mphamvu zonse kumwamba ndi dziko lapansi. (Mateyu 28:18). Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa kosekose iwo akuyandikira Mulungu mwa iye, popeza ali nawo moyo wache chikhaliro wa kuwapembezera iwo (Aheberi 7:25).

KUMWAMBA

Kumwamba ndi kumene Mulungu amakhala ndi ulemerero wache onse. Ambuye Yesu anati: “Pakuti ndipita kukakukonzerani inu malo. Ndipo ndipita kukakukonzerani inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, nanunso mudzakhaleko.” (Yohane 14:2-3).

Kumwamba ndi malo abwino kwambiri kumene Mulungu adzapukuta misozi yonse kuyichotsa pamaso pa ana ake, ndipo sipadzakhalanso imfa, maliro, kulira kapena chowawitsa. Zinthu zoyambazo zapita. Ndipo sipadzakhalanso usiku – chifukwa Ambuye Mulungu adzakhala Kuwala kwawo (Chibvumbulutso 21:4 ndi 22:5).

Kumwamba ali malo Oyera. Ndipo kumwamba sikudzalowa kanthu kosapatulika kapena iye wakuchita chonyasa kapena bodza. Kumwamba kudzalowa iwo wokha olembedwa m'buku la moyo la Mwana wa Nkhosa (Chibvumbulutso 21:27).

Pali njira imodzi yokha yonka kumwamba imene ndi Yesu Khirisitu. Iye anati; “Ine Ndine Nira, khomo, choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine.” (Yohane 14:6). “Ndipo palibe chipulumutso mwa wina aliyense, pakuti palibe **DZINA LINA** pansu pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa munthu limene tiyenera kuzipulumutsidwa nalo.” (Machitidwe 4:12).

TINGAPEZE BWANJI NJIRA YONKA KUMWAMBA

1. Tembenukani mtima, khulupirirani Uthenga wabwino (Maliko 1:15). Kutembenuka mtima ndiko kusiya zoipa zathu zonse ndi kuyamba kutsata Mulungu ndi mtima wathu wonse.

2. Idzani kwa Ambuye Yesu Khirisitu, mwa kupemphera, monga m'mene muliri ndi katundu wamachimo, ndipo mumpemphe iye kuti akhululukire inu. Iye anena: “Ndipo wakudza kwa Ine sindidzamtaya iye kunja.” (Yohane 6:37). “Idzani kwa Ine inu nonse wolema ndi wothodwa ndipo ndidzakupumulitsani.” (Mateyu 11:28).

3. Khulupirirani mwa Khirisitu kuti ndimo muli chipulumutso chani ndipo mwazi wache utusambitsa kutichotsera uchimo wonse (1 Yohane 1:7).

4. Adzakupatsani inu moyo watsopano ... Moyo wosatha. Khirisitu anati; iye wakumva mawu anga, ndi kukhulupirira iye amene anandituma Ine, **ali nawo Moyo Wosatha**, ndipo sadzalowa mkuweruzidwa, koma **wachokera ku imfa, nalowa m'moyo** (Yohane 5:24). Chifukwa chache ngati munthu aliyense ali mwa Khirisitu, ali wolengedwa watsopano, zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano (2 Akorinto 5:17).

5. Mudzakhala ndi mtendere mumtima mwanu, popeza tsono tayedwa olungama ndi chikhulupiriro ndipo tikhale ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khirisitu (Aroma 5:1).

Ndipo umboni nawu, kuti Mulungu anatipatsa ife Moyo Wosatha, ndipo moyo umenewu uli mwa Mwana wache. Iye wakukhala ndi **Mwana ali nawo Moyo**, ndipo wosakhala ndi Yesu aliibe Moyo. Izi ndakulemeberani, kuti mudziwe kuti muli ndi Moyo Wosatha, **inu amene mukhulupirira mu dzina la Mwana wa Mulungu** (1 Yohane 5:11-13).

M'MENE TINGAKHALIRE M'MOYO WATSOPANO

1. Kuwenga Baibulo tsiku ndi tsiku chifukwa ndi chakudya komanso njira yakuunika pa moyo wathu. Lirani mkaka woyenera munga makanda alero, wopanda chinyengo, kuti mukule nawo kufikira chipulumutso (1 Petulo 2:2). Pemphani Mulungu kuti akutsogolereni ndi kukuphunzitsani pamene mulikuwenga mawu ache, mwa Mzimu Woyera.

2. Idzani pafupi ndi Mulungu mwa pemphero tsiku ndi tsiku, kupemphera m'dzina la Yesu. "Musadere nkhalwa konse, komatu m'zonse ndi pemphero, pembedzero ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu, ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse, udzasubga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Yesu Khirisitu." (Afilipi 4:6-7).

3. Yankhulani kwa ena za Yesu Khirisitu. "Mukani kwanu kwa abale ako, nuwauze zinthu zazikulu anakuchitira Ambuye." (Maliko 5:19).

4. M'mayesero, itanani Ambuye. "Pakuti popeza adamva zowawa, poyesedwa yekha, akhoza kuthandiza iwe pamene wayesedwa." (Aheberi 2:18).

5. Ngati mwagwa mtchimo, lapani msanga kwa Mulungu. "Ngati tibvomereza machimo athu kwa Mulungu, ali wokhulupirika ndi wolungama lye, kuti atikhululukire machimo athu ndi kutsambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse." (1 Yohane 1:9).

6. Yesani kukhala wogwirizana ndi okhulupirika ena mwa Ambuye Yesu Khirisitu. "Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzache munga lne ndakondera inu." (Yohane 15:12).

7. Nthawi zonse mverani Mulungu. "Ngati wina akonda lne, adzasunga mawu anga." (Yohane 14:23).

8. MUSAOPE, pakuti Yesu Khirisitu ali ndi inu. "Pakuti lye anati, Sindidzakusiyani konse, kugakhale kukutaya, sindidzakutayani ndithu." (Aheberi 13:5).

9. Dziperekeni nokha kwa thunthu kwa Ambuye Yesu Khirisitu. Lolani lye atsogolere moyo wanu mchifuniro chache, mwakutero tsono mudzapeza chikondwerero choonadi.

Ambuye Yesu Khirisitu ndiye **MPULUMUTSI**, ndipo alinso **MPULUMUTSI** weni- weni. lye ali zonse zimene muzisowa.

The popular "Heart book" with its soul-saving message is obtainable in over 500 languages. Many have found salvation even just by looking at the pictures.

Kindly write to us if you are able to assist us with further translations of our free Gospel literature, informing us of the language into which you could translate this Gospel literature. Your assistance would be appreciated.

If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers. **Our Heart of Man Book can now be downloaded in 480 different languages onto cell phones, tablets, etc from our website www.angp-hb.co.za.**

For **free** Gospel literature, books and tracts in over 540 languages, write to:

E-MAIL: infor@angp.co.za

ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS
P.O. Box 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.

(A Gospel Literature Mission financed by donations)

(Reg. No. 191/001798/08)